

Kulima zomela zamanyowa/zophimba nthaka

Malangizo a alimi ang'ono

Kodi zomela zamanyowa(obiliwila)/mbewu zophimba nthaka n'ciyani?

Zomela zamanyowa/manyowa obiliwila kapena mbewu zophimba nthaka ndi zomela zimalimidwa kuphimba nthaka ndi kubwezeletsa conde.

Kodi n'mapindu ati alipo olima zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka?

Zomela zamanyowa kapena mbewu zophimba nthaka zili n'mapindu kumlimi:

- ▶ Kuteteza nthaka kukokolola, kuwala kwa dzuwa, n'kugwa kwa mvula.
- ▶ Kucepetsa kufala kwa udzu.
- ▶ Kuonjezela conde m'nthaka pogwilitsila nchito zinthu zowolela ndi kuiika/kuthila nitrogen m'nthaka.
- ▶ Kucepetsa kufalikila kwa tulombo ndi matenda.
- ▶ Zakudya za ziweto.
- ▶ Gwelo kopezela ndalama mukagulitsa mbewu zake.
- ▶ Manyowa obiliwila/mbewu zophimba nthaka zozika mizu kwambili zimabweletsa zakudya kucotsa pansi padothi kubweletsa pamwamba kuti mbewu zosazika mizu zidye.

Makhalidwe a zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka

Ngakhale kuti zomela zamanyowa zambili ndi zanyemba (kuiika nitrogen), si zanyemba zonse zili ndi manyowa obiliwila, komabe, zomela zamanyowa abwino kapena mbewu zophimba nthaka.

Munsimu muli mfundo zofunika kuzitsatila posankha mbewu zosewenzetsa monga zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka:

- ▶ Zomela zamanyowa ziyenela kugwilizana n'nyengo yakumaloko, ndi nthaka mobzalamo.
- ▶ Zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka ziyenela kukhala zomela zikula mwamsanga ndi camasamba ambili cigwetsa zowolela zambili.
- ▶ Zomela zamanyowa siziyenela kukhala zofanana ndi mbewu zinalimo kale kapena mbewu zabzalidwa moyandikana nazo cifukwa zingabweletse mpikisano n'kukopa tulombo ndi matenda.
- ▶ Mbewu ziyenela kupezeka mosavuta ndi zochipa.
- ▶ Mbewu iyenela kugwilitsidwa nchito monga manyowa obiliwila iyenela kukhala ndi nitrogen yambili.
- ▶ Zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka ziyenela kusewenzetsa madzi bwino makamaka zikabzalidwa m'madela ouma.

Malangizo molimila zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka



1 Njila yophatikizila mbewu mu ulimi - kodi zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka zizalimidwa pazokha kapena zosakaniza ndi mbewu zina? Njila yophatikizila idzasonyeza kuculuka kwa mbewu, nthawi yobzala ndi kutalikilana/mipata.

2	Kuculuka kwa mbewu (kg/ha)	Mipata (pakati pa mzele x m'mzele) (cm)		Nthawi yobzala		Nthawi yokhwima
		Mbewu imodzi	Mbewu zosiyana	Mbewu imodzi	Mbewu zosiyana	
Nkasi	30 - 50	50 x 20 mpaka 30	Kudalila mbewu yaikulu	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mbewu yaikulu ikafika mnkhongono	4 - 5
Zumba yakuda	25 - 50	Kumwaza	Kukumba pang'ono mumfola mipata ya 20 mpaka 30	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mbewu yaikulu ikafika mnkhongono	3 - 4
Nsansi	40 - 50	75 x 30	Mbewu imodzi mbewu yaikulu, 30cm m'mizele.	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mvula ikugwa bwino. Bzalilani pamodzi.	5 - 6
Zumba yofiila	20 - 25	Kumwaza	Kukumba pang'ono mumfola mipata ya 20 mpaka 30	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mukalima kamodzi (2 - 3) pambuyo pomela mbewu yaikulu	5 - 6
Nyemba	40 - 60	5 x 50 mpaka 75	Pakati pa mzele Kudalila mbewu yaikulu, 5 mpaka 10 cm mipata m' mizele.	Kutha kwa Dec kapena kuciyambi kwa January	Bzalani mbewu yaikulu ikafika mnkhongono	3 - 4

Kuculuka kwa mbewu ndi mipata - kuculuka kwa mbewu zobzala kwa zomela zamanyowa kumasiyana. Thebulo ili pamwambapa isonyeza kuculuka kwa mbewu, mipata, nthawi yobzala ndi nthawi mbewu idzatenga kuti ikhwime ku zomela zamanyowa zodziwika



3 Kupalila/kulima - zomela zamanyowa zambili zimacita bwino kuletsa udzu kumela. Komabe, zomela zisanakule kwambili n' kuphimba nthaka, pangakhale pofunika kulima udzu osacepela kamodzi cabe. Kucepetsa kufunika kolima udzu, onetsetsani kuti mwabzala pafupipafupi kwambili. Komanso, kubzala m'munda woyeletsedwa, mulibe udzu.



4 Kukhwapa zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka - zomela zamanyowa zikayambilila mbewu zazikulu zisanakomoledwe, kukhwapa pamaluwa kapena pamene zowolela zaculuka mokwanila. Kwa manyowa obiliwila obzalidwa monga mbewu payokha, ndibwino kuti kukhwapa kucitike pambuyo pokolola mbewu zake. Zowolela za zomela zamanyowa sizifunika kufocledwa pansi koma kuzisiya pamwamba kuti ziphimbe nthaka.



5 Zomela zamanyowa zopangila zakudya za ziweto - pamene manyowa obiliwila amabzalidwa makamaka kuti aonjezela conde m'nthaka, yambili amakhala cakudya ca ziweto cabwino. Mgwilizano pakati pa kuonjezela conde m'nthaka ndi kudiyetsela ziweto n'zofunika. Ngati zotsalila za zomela zamanyowa ziyenela kudiyetsedwa ku ziweto, cisamalilo ciyenela kukhalapo kuti manyowa a ziweto abwelele kumunda.



6 Zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka ndi kukonzekeletsa nthaka - Kulima zomela zamanyowa ndi njila yabwino yosasokoneza nthaka cifukwa manyowa obiliwila amaphimbila bwino kwambili kupha namsongole/udzu. Zomela zamanyowa zikakhwapidwa ndi kuzisiya kuphimba nthaka/pansi, kugaula pang'ono kosiyana-siyana kungacitike (a) osagaula n'konse (kubzala ndi kalumo/nyankhwino); (b) kukumba maenje a gamphani; ndi (c) kugaula mifolo.



7 Kuteteza zomela zamanyowa/mbewu zophimba nthaka ku moto -pamafunika kupanga malo otchinga (malo palibe kalikonse komela) kuzungulila munda wa manyowa obiliwila kuteteza kumoto.



Promotion of agroforestry supported by:



With support from



by decision of the German Bundestag

Prepared by: Daniel M. Kalala